# NTONDA ZONAL EXAMINATIONS BOARD

## END OF TERM ONE EXAMINATION

# CHICHEWA

(100 Marks)

**Name of Candidate**: ______________________________
(Surname First)
**Name of School**: ______________________________

**GAWO A (Malikisi 30)**

Lembani **CHIMANGIRIZO** pa mutu oti **"MALINGALIRO ANGA"**. Mwazina tsaitirani izi:

**NDIME YOYAMBA**

- Malingaliro anu
- Chifukwa chomwe muli ndi malingalirowo

**NDIME YACHIWIRI**

- Zomwe mukuchita kuti mukwaniritse malingaliro anu
- Zomwe zingalepheretse kukwaniritsa malingaliro anu

**NDIME YACHITATU**

- Zomwe mudzachite mukadzakwaniritsa malingaliro anu

**KAPENA**

Lembani **KALATA** kwa atsibweni anu yowafotokozera za momwe maphunziro anu akuyendera. Mwadzina tsatirani izi?

**NDIME YOYAMBA**

- Sukulu yomwe mumaphunzira
- Momwe maphunziro akuyendera

**NDIME YACHIWIRI**

- Mavuto omwe mukukumana
- Zinthu zomwe atsibweni angakuchitileni kuti maphunziro anu ayende bwino

**NDIME YACHITATU**

- Zomwe mudzachite mukalandira thandizo.

**GAWO B** (Malikisi)

**KUMVETSA NKHANI**

Werengani nkhani ili mmusiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

Mudzi wa mfumu Mwandama adaumanga pa Chigwa kufupi ndi Nkhalankho ya Tandale. Phiri la Mpita limaonekera pang'ono kuseli kwa nkhalango ija. Mfumu Mwandama idali yaimuna, idali ndi ana asanu ndi m'modzi. Wachisamba adali wa mwamuna, dzina lake Maluli. Maluli adali mwana wokondedwa wa mfumu mwandama, adali omvera kwambiri, okonda kucheza ndi anthu, odzichepetsa ndi waluntha lofuna kuphunzira zinthu zambiri. Maluli amakondana kwambiri ndi mlongo wake Namagetsi yemwe adapondana naye. Namagetsi samatha kuphika zinthu osamupatsako mchimwene wakeyo. Maluli akabwera ndi china chofuna kuphika amachipereka kwa Namagetsi.

MAFUNSO.

**a.** Tchulani maina awiri a ana a mfumu?

______________________________

______________________________

**b.** Kodi dzina la mfumu yatchulidwa mnkhaniyi ndi yani?

________________________________

c. Mawu oti "**Wachisamba**" akutanthauzanji munkhaniyi?

________________________________

d. Fotokozani makhalidwe awiri a mwana wa mwamuna wa mfumu munkhaniyi.

___________________________________

___________________________________

_________________________

e. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa:

i. Chigwa: ___________________

ii. Adapondana: _______________

_________________________

f. Kodi dzina loti Tandale lidali la chiyani?

________________________________

g. Tchulani dzina la mwana yemwe adali wokondedwa kwambiri ndi mfumu.

________________________________

h. Perekani mutu wa nkhaniyi.

**4. GAWO C KUPANGA ZIGANIZO** (Malikisi 10)

Pangani ziganizo ndi mawu awa:

a. **Khumutcha**

___________________________________

_____________________________

b. **Chitokosi**

___________________________________

_____________________________

c. **Dzinja**

___________________________________

_____________________________

d. **Mbadwa**

____________________________________

_____________________________

e. **Mpamba**

____________________________________

_____________________________

5. **GAWO D** (Malikisi 40)

**MITUNDU YA MAWU**

1. <u>Kupewa</u> matenda ndi bwino

A. Mlowa m'malo

B. Mneni

C. Dzina

D. Muonjezi

2. Phwando likudikila <u>mkwati</u> kuti abwere.

A. Mfotokozi　C. Mperekezi

B. Muonjezi　D. Dzina

3. Chitagwa kuti <u>phi</u> tonse tidacheuka.

A. Mfotokozi　C. Mfuwu

B. Dzina　D. Mvekero

4. <u>Mayo!</u> Njoka yandiluma.

A. Mneni　C. Mvekero

B. Dzina　D. Mfuwu

5. Iye amayenda <u>mothimbwidzika</u>.

A. Mlumikizi C. Mneni

B. Mfotokozi D. Muonjezi

**Mafunso 6 mpaka 10**. Sankhani mitundu ya mayina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**6.** Amalume azenza <u>mtolo</u> wa nkhuni.

A. Losakhudzika C. Launyinji

B. Lokhudzika D. Lamwinimwini

**7.** Iwo amakhala ku <u>Lilongwe</u>.

A. Lopanda mwinimwini

B. Launyinji

C. Lamwinimwini

D. Losakhudzika

**8.** <u>Mwano</u> supindula.

A. Lokhudzika

B. La mwinimwini

C. Lapadera

D. Launyinji

**9.** Ndipatsireni <u>mpeni</u>

A. Lokhudzika

B. La mwinimwini

C. Lapadera

D. Launjyinji

**10.** <u>Boma</u> linayambitsa sukulu za ulele.

A. Lokhudzika

B. Lopanda mwinimwini

C. Launyinji

D. Losakhudzika

**Mafunso 11 mpaka 15**, Sankhani chachikulu cha zinthu zaperekedwazi

**11.** Mwanapiye

A. Nkhanga C. Buluzi

B. Tambala D. Nkhuku

**12.** Mbululu

A. Nkhano C. Nathasa

B. Chule D. Finye

**13.** Mnyamata

A. Bamboo C. Mwana

B. Kamuna D. Muphwa

**14.** Chiunda

A. Mwanapiye C. Nkhawena

B. Nkhunda D. Nkhukutembo

**15.** Mphonda

A. Mkota C. Msona

B. Mnthoni D. Galu

Mafunso 16 mpaka 20. Sankhani mawu otsutsana mmatanthauzo ndi omwe

atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

16. Mwanayu ndi <u>wamwano.</u>

A. Wochenjera C. Waulemu

B. Wofatsa D. Wodzimva

17. Atate <u>apita</u> ku Phalombe.

A. Agona C. Akhala

B. Afika D. Abwera

18. <u>Mfumu</u> iyi imaweluza bwino milandu.

A. Mdzakazi

B. Mpongozi

C. Mfumakazi

D. Mfumukazi

19. <u>Amayi</u> ali kumunda.

A. Amalume C. Atatavyala

B. Atate D. Mkamwini

20. Agogo ali ndi <u>nkhosa</u> zitatu

A. Mphulu C. Mzidzi

B. Msoti D. Mzambwe

**Mafunso 21 mpaka 25**. Sankhani mawu omwe akusonyeza kuchuluka kwa mawu ali ndi mzere kunsi kwawo.

21. Kuseri kwa nyumba yathu kuli <u>njoka</u>.

A. Njoka C. Manjoka

B. Zinjoka D. Chinjoka

22. Agogo andipatsa <u>mbuzi.</u>

A. Zimbuzi C. Mbuzi

B. Atoned D. Ambuzi

23. <u>Mphunzitsi</u> wa mkulu wapiti ku zomba.

A. Aziphunzitsi C. Maphunzitsi

B. Aphunzitsi D. Tiaphunzitsi

24. <u>Khasu</u> langa lasweka mpini.

A. Makhasu C. Makhatsu

B. Makatsu D. Makasu

25. Mwanapiye wagwera m'madzi.

A. Amwanapiye C. Anapiye

B. Tinapiye D. Tianapiye

**Mafunso 26 mpaka 30**. Sankhani gulu lamayina amawu omwe ali m'musiwa.

26. Anthu.

A. Mu, - A C. Chi, - Zi

B. U, - MA D. Li, MA

27. Khasu.

A. U, - MA C. Ka, - Ti

B. LI, - MA D. KU, - PA,-MU

**28.** Madzi.

A. Chi, - Zi C. I, - Zi

B. Ka, - Ti D. Mu, - Mi

**29.** Kamwana

A. I, - Zi C. Mu, - Mi

B. Ka, - Ti D. Li, - MA

**30.** Zovala

A. Chi, - Zi C. Ka, - Ti

B. I, - Zi D. KU, - PA, - MU

**Mafunso 31 mpaka 35**. Perekani matanthazu azilapi zotsatirazi.

**31.** Mbalame yaikila pa minga.

A. Lilime C. Dzanja

B. Malaya D. Diso

**32.** Miphika yaphulana.

A. Singano C. Chipanda

B. Minga D. Chigule

**33.** Zungulira uku tikumane uko.

A. Mutu C. Ndolo

B. Gaga D.Lamba

**34.** Chimunda chachikulu zokolola m'manja

A. Chingwe C. Tsitsi

B. Maso D. Mtedza

**35.** Kankhalamba kai mvi m'mimba

A. Malambe C. Malalanje

B. Mtedza D. Papaya

**Mafunso 36 – 40**. Zifanifani, malizitsani zifanifani ndi mawu oyenera

**36.** _____ ngati kalulu

A. Kufatsa C. Kuchenjera

B. Kujijirika D. Kupusa

**37.** Kupusa ngati _______

A. Nsima C. Nkhuku

B. Nkhosa D. Nkhumba

**38.** Kutalika ngati _____

A. Kamba C. Nsewu

B. Nsungwi D. Mvula

**39.** Kuwala ngati ________

A. Dzuwa C. Duwa

B. Moto D. Magetsi

**40.** Kukonda m’madzi ngati_____

A. Chitete C. Chule

B. Mwana D. Fisi

## MAFUNSO ATHERA APA!!